# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO


## NTHAMBI YOWONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

## NYENGO MSABATAYI

## KUYAMBIRA PA 17 MPAKA PA 23 NOVEMBER, 2025

### NYENGO M'SABATA IKUBWERAYI

Kuyamba mawa lolemba pa 17 November 2025, tiyembekezere nyengo yofunda, yamitambo ndi yamphepo komanso ya mvula yamabingu yomwe madera ena idzigwa yamphamvu kuyambira kumwera kumafalikira madera akumpoto kwadziko lino. Izi ndi kamba ka nkumano wa mphepo zochokera kumwera komanso zochokera kumpoto zomwe zimatchedwa kuti **ITCZ. Mvula yamphamvu ikuyembekereka m'madera ena makamaka ku mpoto kwa dziko lino, ku Karonga ndi ku NkhataBay, zomwe zikupereka chiopsezo cha madzi osefukira. Mapu ali Kumanja akuonetsa kuchuluka kwa mlingo wa mvula yomwe ikuyembekezereka m'sabata ikudzayi, kuphatikiza mvula ya sabata yonse.** ***Mphepo za Mwera zikuyembekezereka kuomba mwamphanvu pa nyanja zathu kuyambira lachiwiri mamawa pa 18 November 2025.***





*Ulosi wamvula musabata ikudzayi. Kuphatikiza masiku onse musabatayi.*

### NYENGO MU SABATA YANGOTHAYI

Kunali nyengo ya mphepo, yamitambo ndi yotentha komanso mvula yamabingu yomwe m'madera ena inagwa yamphamvu**.** Ku Chintheche ku NkhataBay ndi komwe mvula inagwa yambiri ya mlingo wa **83.2mm** pa **13th November 2025.**

Mapu ali kumanja akuonetsa mvula yomwe inagwa m'sabata yangothayi.




*Mapu akuonetsa kuchuluka kwa mlingo wa mvula m'sabata yangothayi*

### MALANGIZO M'SABATALI

- **Pomwe mvula yamphamvu ikuyembekezereka m'madera ambiri,** tiyeni tikonze njira zonse zodutsa madzi pochotsa zinyalala kuti tipewe madzi osefukira.
- **Mvula yamabingu:** Tikhale m'malo otetezeka
- **Pa nyanja:** Asodzi akupemphedwa kupewa kulowa pa nyanja mphepo ya mphamvu ikamaomba.


***Kuti mudziwe zambiri funsani kwa:*** *The Director, Department of Climate Change and Meteorological Services, Ministry of Natural Resources and Climate Change, P. O. Box 1808, Blantyre, Malawi. Tel: (265) 882 266 579; Email: metdept@metmalawi.gov.mw , Website: www.metmalawi.gov.mw*


**Malo osindikizira: Blantyre** **Yatulutsidwa Lamulungu pa 16 November, 2025**